SABATA LACHITATU: KHRISTU AKONZEKERA NTCHITO YAKE
TSIKU LACHIWIRI: UBATIZO WAKE WA YESU

1. Sabata ino tikuphunzira mmene Khristu anakonzekera ntchito yake. Dzulo tinayamba kuona pa za ubatizo wa Yesu.

Yesu sanabatizidwe ndi chifukwa monga chathu. Kodi chinali chosiyana ndi chiyani pa moyo wa Yesu chomwe chinachita ubatizo wake kukhala wosiyana?

______________________ ______________

Ndi chifukwa chiyani Yesu anabatizidwa?

______________________________________________
==============================================

2. Kusiyana kwake kunali kwakuti Yesu analibe tchimo. Yesu anabatizidwa mmalo mochita chifuniro chonse cha Mulungu. Pali maphunziro ambiri amene ubatizo wa Yesu umatiphunzitsa. Timaona kuti Mulungu Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera anali onse pamodzi pa ubatizowo. Chimenechi ndi chimene tichiphunzire lero.

(1) Mulungu Atate anaonetsedwa mwa mawu wochokera kumwamba.

(2) Mulungu Mwana anali Yesu Khristu mwini wake.

(3) Mulungu Mzimu anaonetsedwa ndi nkhunda imene [illegible]ika kumwamba nitera pa Yesu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga pa Mateyu 3:1[illegible]-17. Kodi Mulungu Atate anaonetsa kukondwera motani ndi zimene anachita [illegible]su?

______________________________________________

______________________________________________
==============================================

3. Iye anaonetsa kukondwera ndi mawu ochokera kumwamba. Pamene Yesu anabatizidwa panachitika zinthu zodabwitsa. Kumwamba kunatseguka.

Mateyu 3:17:
Ndipo onani, mawu akuchokera kumiyamba akuti, "Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa, mwa Iyeyu ndikondwera."

Kodi ndi mawu ayani amene analankhula kuchokera kumwamba?

______________________________________________________________

==================================================================

4. Amenewa anali Mawu a Mulungu. Linali liu la Mulungu Atate. Mulungu ali atatu mwa m'modzi. Ife Akhristu timagwiritsa ntchito mawu polankhula za Mulungu Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Mawu ake ndi a "utatu" amene amatanthauza kuti anthu atatu mwa mmodzi. Akhristu amakhulupirira mwa Mulungu mmodzi. Koma Buku Lopatulika limaphunzitsa kuti kuli Mulungu Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Mulungu ali ndi mbali zitatu kapena anthu atatu. Iye ndi mmodzi, koma alipo atatu mwa mmodzi. Polankhula za Mulungu kaŵirikaŵiri timagwiritsa ntchito mawu a "Utatu" omwe amatanthauza kuti atatu mwa mmodzi.

Kodi ndi chiyani chimaonetsa kuti Mulungu analipo pa ubatizo wa Yesu?

______________________________________________________________

==================================================================

5. Mawu ochokera kumwamba ndiwo amatisonyeza zimenezi. Mawu akuti "Mulungu" amagwiritsidwa ntchito nthaŵi zambiri m'Buku Lopatulika. Nthaŵi zina sitidziŵa ngati amatanthauzadi Mulungu Atate, Mulungu Mwana, kapena Mulungu Mzimu Woyera. Chimenechi ndi chifukwa chakuti Mulungu ndi mmodzi. Kumbukirani kuti ife sitikhulupirira mwa a Mulungu atatu. Ife timakhulupirira mwa Mulungu mmodzi amene ali ndi zigawo zitatu kapena anthu atatu. Tikhoza kuona zigawo zonse zitatu pa ubatizo wa Yesu.

Pa ubatizo wa Yesu, kodi liu lochokera kumwamba linaonetsa gawo liti la utatuwo?

______________________________________________________________

==================================================================

6. Limationetsa ife Mulungu Atate. Mulungu Mwana ndi Mulungu Mzimu analinso pomwepo. Ubatizo wa Yesu ndi wa nthaŵi imodzi pamene gawo la utatu linaonetsedwa.

(1) Kodi Mulungu Atate anaonetsedwa motani?

______________________________________

(2) Mulungu Mwana anali Yesu Khristu mwini.

(3) Mulungu Mzimu Woyera anaonetsedwa mwa nkhunda imene inabwera kwa Yesu.

==========================================================

7. Mulungu Atate anaonetsedwa mwa mawu ochokera kumwamba. Komatu pamenepo sipanali Mulungu Atate yekha. Zigawo za utatu zonse zinalipo pa ubatizowo. Yesu Khristu ndi mmodzi wa utatuwo.

Kodi Khristu ali gawo liti la utatuwo? Kodi Iye ndi Atate, Mwana, kapena Mzimu Woyera?

______________________________________

==========================================================

8. Yesu Khristu Mwana wa Mulungu. Mwina tikhoza kunena kuti Iye ndi Mulungu Mwana. Mulungu Mwana analipo paubatizo wa Yesu. Anali Iye mwini amene anali kubatizidwayo. Kotero gawo la utatu limeneli linalipo.

Popeza magawo a utatuwo analipo pa ubatizowo, kodi Akhristu amakhulupirira mwa a Mulungu atatu kapena mwa Mulungu mmodzi?

______________________________ ____________

==========================================================

9. Ife timakhulupirira mwa Mulungu mmodzi. Iye amachulidwa kuti Atatu mwa mmodzi kapena Atatuwo. Zigawo zonse zitatu za Atatuwo zinalipo pa ubatizo wa Yesu. Pamene Yesu anatuluka m'madzi, kumwamba kunatseguka. Mulungu Atate anaonetsedwa mwa mawu wochokera kumwamba.

Kodi Mulungu Mwana anali yani pa ubatizopo? ____________________

==========================================================

10. Mulungu Mwana ndi Khristu.

Lembani mmene munthu wachiŵiri wa Atatuwo anaonetsedwera pa ubatizo wa Yesu.

(1) Mulungu Atate anaonetsedwa mwa mawu ochokera kumwamba.
(2) Kodi Mulungu Mwana anaonetsedwa motani?

________________________________________

(3) Mulungu Mzimu Woyera anaonetsedwa mwa nkhunda imene inadza kwa Yesu.

===========================================================

11. Mulungu Mwana anali Yesu Khristu mwini. Tsopano taona zigawo ziŵiri za Atatuwo zomwe zinalipo pa ubatizo. Mulungu Atate anali pamenepo Mulungu Mwana anali pamenepo. Iye ndiye anali kubatizidwa. Mulungu Mzimu Woyera analiponso pamenepo.

Mateyu 3:16:

> Ndipo onani, miyamba inamtsegukira Iye, ndipo anapenya Mzimu wa Mulungu wakutsika ngati nkhunda nudza nutera pa Iye.

Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi ndi m'njira yotani imene Mulungu Mzimu Woyera anadzionetsera yekha pa ubatizo wa Khristu?

________________________________________

===========================================================

12. Iye anadzionetsa yekha monga nkhunda. Iye anatsika monga nkhunda ndi kudzatera pa Yesu. Nkhunda ndi yaukhondo ndi yofatsa. Munthu mmodzi wa Atatuwo pa ubatizo wa Yesu anadzionetsa yekha monga nkhunda.

Kodi ndani anatsika kuchokera kumwamba monga nkhunda ndi kudzatera pa Yesu?

________________________________________

===========================================================

13. Iye anali Mzimu Woyera amene anadza m'njira yotere. Iye anabwera kwa Yesu. Iye anatera pa Yesu. Chimenechi chinaonetsa kuti Mzimu Woyera anadza mwa Iye ndi kukhala naye.

Lembani munthu wachitatu wa Atatuwo amene anaonetsedwa pa ubatizo wa Yesu.

(1) Mulungu Atate anaonetsedwa mwa mawu ochokera kumwamba
(2) Mulungu Mwana anali Yesu Khristu mwini.
(3) Kodi Mulungu Mzimu Woyera anaonetsedwa motani?

________________________________________

==================================================================

14. Mzimu Woyera anaonetsedwa mwa nkhunda imene inadza kwa Yesu. Pa ubatizo wa Yesu a Mulungu Atatu anaonetsedwa. Komatu simalo okhawo amene amalankhulidwa za umodzi. Yesu mwini analankhula za utatuwo asanachoke pa dziko lapansi.

Mateyu 28:18-19:

Ndipo Yesu anadza nalankhula nawo, nanena, "Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine kumwamba ndi dziko lapansi. Chifukwa chake mukani, mphunzitsani anthu amitundu yonse, ndi kuŵabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera."

Lembani mmene anthu aŵiri oyamba mwa Atatuwo anadzionetsera pa ubatizo wa Khristu.

(1) Kodi Mulungu Atate anaonetsedwa motani?

________________________________________

(2) Kodi Mulungu Mwana anaonetsedwa motani?

________________________________________

==================================================================

15. Atate anaonetsedwa mwa mawu ochokera kumwamba. Mulungu Mwana anali Yesu Khristu mwini.

Kodi munthu wachitatu mwa atatuwo anadzionetsa motani pa ubatizo wa Yesu?

________________________________________

16. Mulungu Mzimu Woyera anaonetsedwa mwa nkhunda imene inatsika nitera pa Yesu. Yesu analankhula za Utatuwo kwa ophunzira ake. Iye anati iwo adayenera kumauza ena za mmodzi mwa Atatu. Iye anati anayenera kugwiritsa ntchito maina a Mulungu Atatuwo pamene iwo ali kubatiza anthu. Iwo ayenera kubatiza anthu m'dzina la Atate ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera.

Kodi Akhristu amakhulupirira mwa Mulungu mmodzi kapena mwa a Mulungu atatu?

________________________________________

Fotokozani chifukwa chimene kulili maina atatu?

________________________________________

==========================================================================

17. Tidzalankhula za izi m'kalasi. Maina atatuwo amaonetsa zigawo zitatu kapena umunthu utatu wa Mulungu.

Lembani mmene umunthu ulili wonse wa Atatuwo unaonetsedwa pa ubatizo wa Yesu.

(1) Kodi Mulungu Atate anaonetsedwa motani?

________________________________________

(2) Kodi Mulungu Mwana anaonetsedwa motani?

________________________________________

(3) Kodi Mulungu Mzimu Woyera anaonetsedwa motani?

________________________________________

==========================================================================

SABATA LACHITATU: KHRISTU AKONZEKERA NTCHITO YAKE
TSIKU LACHITATU: MAYESERO A YESU

1. Dzulo tinaphunzira zigawo zitatu za Utatuwo.

Lembani mmene munthu aliyense anaonetsera Utatu wao pa ubatizo wa Yesu.

(1) Kodi Mulungu Atate anaonetsedwa motani?

______________________________

(2) Kodi Mulungu Mwana anaonetsedwa motani?

______________________________

(3) Kodi Mulungu Mzimu Woyera anaonetsedwa motani?

______________________________

==========================================================

2. Mulungu Atate anaonetsedwa mwa mawu ochokera kumwamba. Mulungu Mwana anali Yesu Khristu mwini wake. Mulungu Mzimu Woyera anaonetsedwa kupyolera mwa nkhunda imene inatsika nitera pa Yesu. Yesu atangotha kubatizidwa Mzimu Woyera anamutsogolera Iye kuchipululu. Kumeneko Iye anayesedwa ndi Satana ndipo Satana anamuyesa kuti achimwe. Lero tiphunzira mayesero atatu amene Satana anaŵabweretsa.

(1) Kuti Yesu asandutse miyala kuti ikhale mkate.
(2) Kuti Yesu adziponye yekha kuchokera pamwamba pa kachisi.
(3) Kuti Yesu agwade pansi ndi kupembedza Satanayo.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 4:1 mpaka 11. Kodi Yesu anali kuchita chiyani kwa masiku makumi anayi usiku ndi makumi anayi usana m'chipululu?

______________________________

==========================================================

3. Yesu anasala kwa masiku makumi anayi. Iye anatsogozedwa ndi Mzimu Woyera ku chipululu. Chimenechi chimaonetsa kuti chinali chifuniro cha Mulungu kuti Iye ayesedwe. Iye anakhala kumeneko masiku makumi anayi usana ndi usiku. Pa nthaŵi imeneyi Iye sanadye kanthu.

Kodi mukuganiza kuti Yesu anamva bwanji atakhala nthaŵi yonseyi osadya?

______________________________________________________________

================================================================

4. Iye anayenera kukhala ndi njala yaikulu ndipo anali wofooka kwambiri ndithu. Inali nthaŵi imeneyi pamene Satana anabwera kwa Iye. Satana anadziŵa kuti Yesu anali ndi njala kwambiri.

Mateyu 4:3:
Ndipo woyesayo anafika nanena kwa Iye, "Ngati muli Mwana wa Mulungu, tauzani kuti miyala iyi ikhale mikate."

Kodi Satana anayesa Yesu kuti asandutse miyala ikhale chiyani?

____________________________

================================================================

5. Iye anayesa Yesu kuti atembenuze miyala kuti ikhale mikate. Yesu nkuti asanadye kanthu kalikonse kwa masiku makumi anayi. Satana anadziŵa kuti Iye anali ndi njala koma Yesu sanavomereze kuchita zomwe Satana ananena. Kodi Yesu anali nayo mphamvu yopangira chakudya? Inde! Nthaŵi ina Yesu pamene anali ndi moyo anadyetsa anthu zikwi zisanu ndi mikate isanu ndi nsomba ziŵiri. Yesu anali ndi mphamvu yochita zozizwitsa. Koma Iye sanafune kugwiritsa ntchito mphamvuyo kuti adzilemekeze yekha.

Mateyu 3:4:
Koma Iye anayankha nati, "Kwalembedwa, munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi mawu onse akutuluka mkamwa mwa Mulungu."

Kodi ndani anayesa Yesu kuti asandutse miyala kukhala mikate?

___________________________________________________________

================================================================

6. Satana ndiye anachita zimenezi. Yesu anali ndi njala kwambiri ndipo anali kufuna chakudya. Koma Iye anadziŵa kuti kumvera Mawu a Mulungu ndi kofunika koposa chakudya. Iye anadziŵa kuti Mulungu sanafune kuti

gwiritse ntchito mphamvu kwa Iye yekha.

Yesero limeneli likutiuza kuti kutsata Mawu a Mulungu ndi kofunika kwambiri. Ndikofunika koposa kukhutitsa zikhumbitso za matupi athu. Yesu anaonetsa zimenezi pamene anali kuyankha Satana. Iye anati, "munthu sakhala ndi moyo ndi mkate wokha." Chakudya, madzi ndi zovala sizosoŵeka zathu zokha ayi. Tiyenera kumvera Mulungu.

Kodi ndi yesero liti limene limaphunzitsa kuti kumvera

Mulungu ndi kofunika koposa kukhutitsa zosoŵa za matupi athu?

______________________________________________________________

==================================================================

7. Ndi yesero losandutsa miyala kuti ikhale mkate. Ifenso timayesedwa ndi Satana. Mwina ife tikhoza kuyesedwa kuti tikhale osapita ku tchalitchi pa sabata. Mwina tikhoza kufuna kukagwira ntchito kumunda mmalo mopita ku tchalitchi. Munthu amene amachita zimenezi poyamba amaika zofuna za thupi lake. Buku Lopatulika limanena kuti tiyenera kukomana ndi Akhristu ena. Tiyenera kugwiritsa ntchito tsiku la sabata kuti likhale tsiku lopembedza. Tiyenera kuika Mawu a Mulungu kuti akhale oyamba m'moyo mwathu. Chimenechi ndi chimene Yesu anachita.

Kodi yesero loyamba limene Satana anapatsa Yesu ndi lotani?

(1) ______________________________________________________

(2) Kuti Yesu adziponye yekha pansi kuchokera pamwamba pa Kachisi.
(3) Kuti Yesu agwade pansi ndi kupembedza Satana.

==================================================================

8. Yesero loyamba linali lakuti Yesu asandutse miyala kukhala mikate. Yesu anakana kuchita zimenezi. Iye anagwiritsa ntchito Mawu a Mulungu pomuyankha Satana. Ndipo Satana anamtengera Iye pamwamba pa kachisi.

Mateyu 4:6:
Nanena naye, "ngati muli Mwana wa Mulungu, kudzigwetse nokha pansi.

Ngati Yesu akadadziponya pansi ndipo osapweteka, kodi anthu akananena chiyani za Iye?

______________________________

==============================================================

9. Anthu akananena kuti Iye anali munthu wodabwitsa. Mwina iwo akadayamba kumutsata Iye. Limeneli linali yesero lolimba kwa Yesu. Satana anagwiritsa ntchito ndime yochokera m'Chipangano Chakale pofuna kuti yeserolo likhale lolimba. Iye ananena kuti:

Mateyu 4:6:

> Pakuti kwalembedwa, "adzauza angelo ake za iwe, ndipo pa manja awo adzakunyamula iwe, ungagunde konse phazi lako pamwala. "Yesu ananena naye, "ndiponso kwalembedwa, usamuyese Ambuye Mulungu wako."

Pamene Satana anayesa Yesu kuti adzigwetse yekha pansi, kodi Yesu analola?

______________________________

==============================================================

10. Yesu sanavomere. Iye sanamvere yesero limeneli. Yesu anagwiritsa ntchito Mawu a Mulungu pomuyankha Satana. Iye anati, "kwalembedwa kuti, usamuyese Ambuye Mulungu wako." Kodi pamenepa Yesuyu anatanthauza kuti Satana asamuyese, ayi. Yesu anatanthauza kuti, Iye, Yesu mwini sayenera kuyesa Mulungu Atate. Ndime zimene Satana anagwiritsa ntchito zinali zakuti angelo a Mulungu adzachinjiriza Yesu kuti asapweteke. Koma anadziwa kuti sanayenera kuchita zinthu zopusa. Iye sanayenere kuvutitsa Mulungu kuti amupulumutse kuchokera pakudzigwetsa.

Kodi ndi yesero liti la Yesu limene limatiphunzitsa kuti sitiyenera kuyesa Mulungu m'njira zopusa?

______________________________

==============================================================

11. Linali yesero lodzigwetsa yekha pansi kuchokera pamwamba pa kachisi. Satana anafuna kuti Yesu amumvere. Iye anafuna kuti Yesu achite zinthu zina zopusa ndi kuyesa Mulungu. Satana amatinyenganso mu njira imeneyi. Iye amafuna kuti ife tizichita zinthu zopusa ndi kuyesa Mulungu. Iye amafuna kuti tizidzipweteka tokha.

Kudzigwetsa yekha pansi kuchokera pamwamba pa kachisi linali yesero lina la Yesu lachiŵiri. Kodi loyamba linali lotani? ______

______

==================================================================

12. Yesero loyamba linali lakuti Yesu asandutse miyala kuti ikhale mikate. Izi zidatiphunzitsa kuti ndi bwino kwambiri kumvera Mulungu koposa kukhutitsa matupi athu. Yesero lachiŵiri limatiphunzitsa kuti sitiyenera kuyesa Mulungu m'njira yopusa. Mulungu analonjeza kutisamalira. Pamene tili paulendo tikhoza kumupempha Mulungu kuti atisamalire. Koma sitiyenera kumuyesa Iye poyendetsa galimoto mwaliŵiro kwambiri kapena kukhala osasamalira.

Kodi yesero lachiŵiri la Yesu linali lotani?

(1) Kuti Yesu asandutse miyala kukhala mikate.
(2) ______
(3) Kuti Yesu agwade pansi ndi kupembedza Satana.

==================================================================

13. Yesero lachiŵiri linali lakuti Yesu adzigwetse yekha pansi kuchokera pamwamba pa kachisi. Koma Yesu anakana. Ndipo Satana anapita naye ku phiri lalitali.

Mateyu 4:8-9:

> Pomwenso mdierekezi anamuka naye ku phiri lalitali, namuonetsa maiko onse a dziko lapansi ndi ulemelero wawo; nati kwa Iye, "zonse ndidzakupatsani inu ngati mudzagwa pansi ndi kundigwadira ine."

Kodi Satana anafuna kuti Yesu achite chiyani? ______

______

==================================================================

14. Satana anafuna kuti Yesu agwe pansi ndi kumupembedza iye. Satana ana na kuti iye adzampatsa Yesu maufumu onse a dziko lapansi. Kodi Sat n akadakhoza kuchita chimenechi? Iye akadakhoza kuchita kwa ka nt' i kochepa. Satana ndiye olamulira wa dziko lino tsopano. Mwina i chikukudabwitsani. Koma taganizirani maiko a dziko lino lapansi. ambiri aiwo amatsata Khristu? Ayi, iwo amatsata zilakolako zawo.

Kodi tiyenera kupembedza yani mmalo mwa Satana?

---

15. Tiyenera kupembedza Mulungu. Chimenechi ndi chimene Yesu anauza Satana pamene iye anamuyesa. Iye anakana kuti agwe pansi ndi kuti apembedze Satana.

Mateyu 4:10:

> Pomwepo Yesu ananena kwa iye "choka Satana, pakuti kwalembedwa, Ambuye Mulungu wako udzamgwadira ndipo Iye yekha udzamlambira."

Kodi Satana ananena kuti adzamupatsa chiyani Yesu ngati akadamupembedza?

---

16. Iye ananena kuti adzamupatsa Iye maufumu a dziko lapansi. Koma Yesu anakana kupembedza Satana. Iye anadziŵa kuti anayenera kupembedza Mulungu. Iye anadziŵa kuti ife sitiyenera kutembenuka kuchoka kwa Mulu-chifukwa cha china chilichonse.

Kodi yesero la Yesu limene limatiphunzitsa kuti sitiyenera kutembenuka ndi kusiya kupembedza Mulungu ndi lotani?

---

17. Ndi yesero logwada pansi ndi kupembedza Satana. Yesero la mtundu omwewu limabweranso kwa ife. Satana amatiyesa ife ndi zinthu zosiyana-

siyana. Iye amayesa Akhristu ena ndi ndalama. Iye amanena kuti, ngati uli Mkhristu siungathe kukhala olemera chifukwa simungathe kunyenga anthu. Simungathe kulandira ziphuphu. Siya Chikhristu ndipo udzalemera. Satana amanyenga Akhristu ena ndi mphamvu. Iye amanena kuti, Mkhristu sangakhale sing'anga wokhwima. Siya Chikhristu ndipo ine ndidzakupatsa mphamvu yopambana anthu ena."

Kodi mayesero aŵiri oyamba a Yesu anali otani?

(1) ______________________________

(2) ______________________________

(3) Kuti Yesu agwade pansi ndi kupembedza Satana.

==========================================================

18. Mayesero oyamba anali aŵiri akuti, (1) Yesu asandutse miyala kukhala mikate. (2) Kuti Yesu adzigwetse yekha kuchokera pamwamba pa kachisi.

Kodi yesero lachitatu la Yesu linali lotani? ______________________________

______________________________

==========================================================

19. Yesero lachitatu linali lakuti Yesu agwe pansi ndi kupembedza Satana. Yesu anakana mayesero a Satana. Ifenso tiyenera kumukanira Iye. Ife sitiyenera kusiya njira ya Chikhristu. Timayenera kumvera Mulungu mu zilizonse.

Mwina inu mwaphunzira kanthu kena katsopano mphunziro limeneli: Lembani chomwe muli kuchiganizira kuti ndi chiphunzitso chofunika mphunziro limeneli.

______________________________

______________________________

==========================================================

20. Tidzakambirana za zimenezi tonse limodzi.

Kodi mayesero atatu amene Satana anaŵabweretsa kwa Yesu ndi otani?

(1) ______________________________________________

(2) ______________________________________________

(3) ______________________________________________

========================================================================

SABATA LACHITATU: KHRISTU AKONZEKERA NTCHITO YAKE
TSIKU LACHINAYI: MAYESERO A YESU AMATITHANDIZA

1. Dzulo tinaphunzira za mmene Yesu anayesedwera ndi Satana.

Kodi ndi mayesero atatu otani amene Satana anaŵabweretsa kwa Yesu?

(1) ____________________

(2) ____________________

(3) ____________________

==========================================================================

2. Mayeserowo anali akuti, (1) Yesu asandutse miyala kuti ikhale mkate. (2) Kuti Yesu adziponye yekha pansi kuchokera pamwamba pa kachisi. (3) Kuti Yesu agwade pansi ndi kupembedza Satana. Yesu anagonjetsa mayesero a Satana. Iye anaŵagonjetsa iwo m'chipululu. Ndipo anaŵagonjetsa nthaŵi ya moyo wake. Mayesero a Yesu ndi otithandiza kwambiri ife. Lero tiphunzira mmene tingagonjetsere mayesero monga mmene Yesu anachitira.

(1) Tiyenera kufunsa Yesu kuti atithandize.
(2) Tiyenera kugwiritsa ntchito Mawu a Mulungu.

Dzulo tinaphunzira za mayesero a Yesu kuchokera m'Buku la Mateyu. Lero tiwerenga za zimenezi kuchokera m'buku la Luka. Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 4:1 mpaka 13. M'ndime zimenezi, kodi ndi nthaŵi zingati zimene Yesu anakhala ali kukana Satana?

____________

==========================================================================

3. M'ndime zimenezi Yesu anamukana katatu. Yesu anakana Satana nthaŵi iliyonse imene anali kumuyesa. Satana ndi mdani wa Mulungu. Pamene Mwana wa Mulungu anabadwa, Satana anayesetsa kuti amuphe. Muli kukumbukira kuti iye anafuna kupha Yesu ali wakhanda kupyolera mwa Herode. Koma Mulungu ndiye anapulumutsa moyo wake wa Yesu. Pamene Yesu anali munthu, Satana anayesetsa kumulepheretsa ntchito yake. Iye anafuna kuti Yesu amumvere.

Kodi Yesu anamvera mayesero a Satana?

________________________________

==========================================================================

4. Yesu anagonjetsa mayesero. Iye sanachite zomwe Satana anamuuza kuti achite. Yesu adagonjetsa Satana pogwiritsa ntchito Mawu a Mulungu Yesu anagwiritsa ntchito Mawu a Mulungu pa nthaŵi iliyonse imene Satana anali kumuyesa. Koma Satana sanaleke kumuyesabe Yesu. Iye anali kubwera kaŵiri kwa Yesu pamene anali ndi moyo pa dziko lapansi. Iye anafuna kutembenuza Yesu kuti asiye ntchito yake. Koma Yesu sanamvere mayesero a Satana.

Kodi Yesu anachitapo tchimo pamene anali ndi moyo pa dziko lapansi pano?

________________________

==========================================================================

5. Yesu sanachite tchimo mpang'ono pomwe. Iye anagonjetsa yesero lililonse la Satana. Taona kuti pamene munthu akhala Mkhristu, amatembenuka ndi kusiya machimo ake. Kodi zimenezi zimatanthauza kuti iye sadzayesedwanso? Ayi sizitanthauza chomwecho. Satana amapitirizabe kumuyesa munthu ngakhale pamene ali Mkhristu. Yesu anali kuyesedwa pa moyo wake wonse padziko lapansi. Inali nthaŵi yochepa yokha imene Satana anali kumusiya.

Luka 4:13:
> Ndipo mdierekezi, mmene adamaliza mayeso onse, analekana naye kufikira nthaŵi ina.

Yesu sanabatizidwe chifukwa cha zolinga monga zathu. Kodi ndi chiyani chinali chosiyana pa moyo wa Yesu chomwe chinapangitsa ubatizo wake kukhala wosiyana?

________________________________

==========================================================================

6. Yesu sanachimwe. Chifukwa cha ichi Yesu sanabatizidwe ndi chifukwa cha tchimo monga ife. Nthaŵi zina Mkhristu akhoza kuchimwa pamene iye asakufuna kuti achimwe. Iye ayenera kukondweretsa Mulungu. Kodi kuli thandizo kwa Mkhristu amene ali kumenyana ndi mayesero a Satana? Inde, thandizo lilipo. Yesu akhoza kumuthandiza.

Kodi Mkhristu masiku ano akakhala pa mayesero akhoza kupeza thandizo kwa Yesu motani?

_______________________________________________

==================================================================

7. Iye akhoza kupempha thandizo kwa Yesu. Iye akhoza kupemphera. Kumbukirani kuti pali wina wake amene anakhala padziko lapansi yemwe anali kuyesedwa kaŵirikaŵiri. Koma iye sanachimwe. Munthu ameneyu anali Yesu. Iye amadziŵa mmene Satana amatiyesera kuti tisatsatire Mulungu. Iye amadziŵa kuti kugonjetsa mayesero a Satana ndi kovuta. Iye amamvetsetsa mmene ife timavutikira pamene tikumenyana ndi mayesero ndipo akhoza kutithandiza. Ife tikhoza kulandira chithandizo cha Yesu kupyolera mwa mapemphero. Yesu akhoza kutithandiza chifukwa Iye mwini anayesedwa.

Ahebri 2:18:

> Pakuti popeza adamva zoŵaŵa, poyesedwa yekha akhoza kuthandiza iwo amene ayesedwa.

Kodi Yesu anayesedwa koposa kamodzi pa nthaŵi imene anali ndi moyo pa dziko lapansi?

_______________________________________________

==================================================================

8. Yesu anayesedwa nthaŵi zambiri. Iye anagonjetsa mayesero onse. Ife tikhoza kugonjeza mayesero mwa mapemphero. Kupemphera ndi kulankhulana ndi Mulungu. Yesu tsopano ali ndi Mulungu Atate. Iye amamva mapemphero athu. Iye akhoza kutithandiza pemene tili kuyesedwa. Njira imeneyi ndi imene ife tingagonjetsere:

(1) Tiyenera kupempha Yesu kuti atithandize.
(2) Tiyenera kugwiritsa ntchito Mawu a Mulungu.

Kodi ndani amene akhoza kumva mapemphero athu. _______________

==================================================================

9. Yesu amamvetsetsa za mayesero athu. Iyenso anali kuyesedwa. Thomasi ndi Mkhristu watsopano. Iye asanakhale Mkhristu, anali kuba zinthu zambiri. Tsopano iye ali kudziŵa kuti kuba ndi tchimo. Thomasi anafulatira ku tchimo lake. Koma iyeyu waona buku limene ahali kulifuna kwambiri koma alibe ndalama zogulira bukulo. Ndipo akuganiza kuti njira yapafupi ndiyo yongoba bukuli. Satana ali kumuyesa mayeso.

Kuchokera pa zimene taphunzirazi, kodi Thomasi ayenera kuchita chiyani kuti agonjetse yesero limeneli?

______________________________

===========================================================================

10. Thomasi ayenera kupempha Yesu kuti amuthandize. Njira ina yachiŵiri yogonjetsera mayesero ndi yogwiritsa ntchito Mawu a Mulungu. Taphunzira zifukwa zimene ife tiyenera kuphunzirira moyo wa Khristu. Cholinga chimodzi ndi chakuti tikhoza kutsata chitsanzo chake. Ife timafuna kukhala monga Yesu. Kodi Yesu m'chipululu anali kuyankha mayesero a Satana motani? Satana anayesa Yesu katatu. Yesu anayankhanso pogwiritsa ntchito Mawu a Mulungu. Ife timafuna kupambana mayesero. Tsono tiyeni tizitsata chitsanzo cha Yesu pamene tikuyesedwa, tiyeni tizigwiritsa ntchito Mawu a Mulungu.

Kodi ndi buku liti limene timapezamo Mawu a Mulungu? ______________

______________________________

===========================================================================

11. Timapeza Mawu a Mulungu m'Buku Lopatulika. Ngati titsata chitsanzo cha Yesu tidzayankha Satana ndi Mawu a Mulungu. Koma ife sitidziŵa nthaŵi imene Satana angatiyese. Koma izi zikutanthauza kuti Mkhristu azinyamula Buku Lopatulika nthaŵi zonse? Zimenezi sizimene akutanthauza. Yesu sanali kuwerenga m'Buku pofuna kumuyankha Satana. Iye anaphunzira Mawu a Mulungu kuyambira ali mnyamata wamng'ono. Iye anadziŵa bwino mawuŵa naŵaika mumtima mwake ndi m'maganizo ake.

Kodi ife tikhoza kudziŵa Mawu a Mulungu m'Buku Lopatulika motani?

______________________________

===========================================================================

12. Timadziŵa mawuwo powerenga ndi poŵaphunzira. Ife sitingathe kugwiritsa ntchito Mawu a Mulungu potsutsana ndi Satana ayi koma pokhapokha titaŵadziŵa. Timayenera kuwaphunzira tsiku ndi tsiku. Imeneyi sintchito yapafupi ayi. Koma ngati tili kufuna kukula ndi mphamvu ndi kugonjetsa Satana tiyenera kugwira ntchito imeneyi. Tiyenera kuigwira tsiku ndi tsiku.

Kodi chinthu choyamba chomwe tiyenera kuchita pofuna kugonjetsa mayesero ndi chiyani?

(1) ______________________________

(2) Tiyenera kugwiritsa ntchito Mawu a Mulungu.

===========================================================

13. Poyamba tiyenera kupempha Yesu kuti atithandize ife. Tiyeneranso kugwiritsa ntchito Mawu a Mulungu. Ganizirani za msilikali ali kupita kukakomana ndi mdani. Iye amakhala okonzekera nkhondo. Iye amavalira-tu zovala zake zankhondo ndi chisoti. Koma dikirani! Kodi iye ali ndi lupanga? Ngati alibe lupanga, sanakonzekere nkhondo.

Mtumwi Paulo amanena kuti Akhristu ali monga asirikali. Ife tiyenera kukhala okonzekera kukomana ndi mdani wathu, Satana. Mawu a Mulungu ndi mawu athu.

**Aefeso 6:17:**

Mutengenso chisoti cha chipulumutso, ndi lupanga la Mzimu ndilo mawu a Mulungu.

Kodi Yesu anali kugwiritsa ntchito chiyani pofuna kuyankha mayesero a Satana?

______________________________

===========================================================

14. Yesu anali kugwiritsa ntchito Mawu a Mulungu ndipo anatipatsa chitsanzo.

Mariya ndi Mkhristu. Makolo akenso ndi Akhristu. Makolo ake anamuuza kuti asamapite kubawa kuti akamwe moŵa. Usiku wina bwenzi la Mariya anati, "Tiye tipita kubawa tikamwe kuti tikasangalala." Mariya sanafune kuŵakanira abwenzi akewo. Komabe anali kukumbukira kuti Buku Lopatulika limanena kuti, "lemekeza atate ako ndi amako." Iye anadziŵa kuti sakadalemekeza makolo ake ngati apita kubawako ndipo iye sanapita. Iye anagonjetsa yesero limeneli.

Kodi Mariya anagwiritsa ntchito chiyani pofuna kugonjetsa yeso limeneli?

______________________________

===========================================================

15. Mariya anagwiritsa ntchito Mawu a Mulungu. Iye anachita monga Yesu anachitira. Pamene ife tikuyesedwa, timagwiritsa ntchito zomwe timadziŵa za Mawu a Mulungu pa kumenyana ndi Satana. Ngati ife tikudziŵa Mawu a Mulungu tikhoza kudziŵa mmene tingakhalire. Tikhoza kudziŵa kuti tchimo ndi chiyani. Timadziŵa kuti kutsatira Yesu kumatanthauza chiyani.

Masalmo 119:11:
Ndinawabisa mawu anu mumtima mwanga, kuti ndisalakwire Inu.

Kodi Mkhristu anayenera kuphunzira chiyani kuti akhale okonzekera kumenyana ndi mayesero a Satana?

______________________________

================================================================

16. Ife tiyenera kuphunzira Buku Lopatulika. Tiyenera kuloŵeza mawu. Iye ayenera kudziŵa zomwe zili m'ndime zina zomwe iye asanawaloweze.

Kodi chinthu chachiŵiri ndi chiti chimene ife tiyenera kuchita pofuna kugonjetsa mayesero?

(1) Tiyenera kupempha Yesu kuti atithandize.

(2) ______________________________

================================================================

17. Ife tiyenera kugwiritsa ntchito Mawu a Mulungu. Tiyenera kupatsa Satana mayankho ochokera m'Buku Lopatulika. Ife tiyenera kudziŵa zomwe Buku Lopatulika limanena.

Kodi inu mumagwiritsa ntchito njira yotani pophunzira Buku Lopatulika?

______________________________

================================================================

18. Tidzakambirana tonse zimenezi.